NYA_TTB_1108_SCRIPT

1 Yohane : 4:12-21

Mutu : Wokhulupirira ayenera kukondana wina ndi mnzake

Moni waKumwambakwainu wokondedwa anzanga apaulendo. Lero ndi tsiku labwino momwe Ambuye afuna kutitsogolera ndi mau apa Ahebri 13:5-6, amene akuti, “Sindidzakusiya konse, kungakhale kukutaya, sindidzakutaya ndithu. Kotero kuti tinena molimbika mtima, mthandizi wanga ndiye Ambuye; sindidzaopa; adzandichitira chiyani munthu?”

Tsono mupologalamu yapita ija, tinali kusanthula 1 Yohane 4:7-11, pa mutu wakuti akristu ayenera kukondana wina ndi mnzake. Ndipo lero pa 1 Yohane 4:12-21, tipitiliza mutu womwewo wakuti wokhulupirira ayenera kukondana wina ndi mnzake.

12. Palibe munthu adamuona Mulungu nthawi ili yonse; tikakondana wina ndi mnzake, Mulungu akhala mwa ife ndi chikondi chikhala changwiro mwa ife.

Tiyeni pano tiyambe ndi kugwira mau akuti, “Palibe munthu adamuona Mulungu nthawi ili yonse.”Pamau amenewa, anthu ena akhala akutsutsa kotero kuti akhala akupereka zitsanzo za anthu

amene adaona Mulungu.Iwo, amapereka zitsanzo za Adamu ndi Mose amene anali kulankhula ndi Mulungu maso ndi maso ndipo kuti anabisalam'phanga la miyala. Komanso pali chitsanzo china pa Yesaya 6:1, pamene Yesaya mwini akuchitira umboni wakuti, "Chaka chimene mfumu Uziya anafa, ndinaona Ambuye atakhala pa mpando wachifumu wautari, ndi wotukulidwa, ndi zobvala zake zinadzala m'Kachisi." Ezekieli naye anaona masomphenya a Mulungu ndipo Mulungu adaonekeransokwa Danieli ndi anzake. Koma mwa zitsanzo zonsezi, Yohane m'Chipangano Chatsopano akunena kuti, "Palibe adaona Mulungu panthawi ili yonse."Kodi mau a Mulungu amatsutsana?Yankho likuti ayi, mau a Mulungu satsutsana ndipo sikudzatheka kutero. Ndiye tikaonetsetsa tipeza kuti Yohane sadalekeze mau ake pomwepo, koma adapitiliza kunena pa Yohane 1:18, kuti, "Mwana Wobadwa yekha wakukhala pa chifuwa cha Atate, Iyeyu anafotokonzera." Kutanthauza kuti Mwana Wobadwa yekha, Yesu Kristu ndiye amene anaonetsa nkhope ya Mulungu. Tikunena kuti Yohane wachita kafukufuku ndipo wapeza kuti pamene Mulungu anali kuonekerakwa anthu, m'Chipangano Chakale, sanali kuona Mulungu, popeza Mulungu ndiMzimu. Umu, ndimomwe inu ndi ine, timampembedzera.Ndiye

tikunena kuti Mulungu anali kuonekeram'chithunzi cha mtundu wina, kotero kuti sadadzionetserem'chithunzichake cheni-cheni ayi.Tsono Mtumwi Yohane akunenetsa kuti palibe munthu adaona Mulungu ngakhale pamene Ambuye Yesu anakwera Kumwamba.Koma taonani pa Yohane 14:9, Ambuye Yesu akumuuza Filipo, kuti, "Iye amene waona Ine, waona Atate; unena iwe bwanji, mutionetsere Atate?"Kutanthauza kuti nthawi iyi, mkuti anthu anali kuona Mulungu amene anabisika m'thupi la munthu, kotero kuti anthu ambiri sadamzindikire Iye. Tikunena kuti Iye anakula mwa munthu mumzindawa Nazarete, kotero kuti anthu sanamdziwe kuti anali Mwana wa Mulungu. Kutsimikiza kuti palibe munthu amene anaona Mulungu m'maonekedwe ake-ake kufikira lero lino.

Wokondedwa anzanga apaulendo, chomwe Mtumwi Yohane akunena pano ndichakuti palibe munthu amene adaona Mulungu nthawi iliyonse. Koma akunenetsa kuti lero lino Mulungu akhoza kuonekerakwa inu ndi ine, pamene akristu akondana wina ndi mnzake. Ndiye popeza dziko pakali pano, silingaone Yesu monga momwe akuonetsedwera m'mau a Mulungu, koma dziko

likhozakuona chikondi cha Mulungu kudzera m'moyo wa wokhulupirira popeza ndiwo aimira Iye. Tikunenetsa pano kuti palibe m'modzi wa ife amene adaona chikondi cha Mulungu kufikira pamene Mulungu mwini adachionetsa yekha pamtanda pamene Ambuye Yesu anafa. Ndipo lero lino Mulungu yemweyu akuonetsa chikondi chake kudzera mwa Mzimu Woyera.Ichi, ndichimene Mtumwi Paulo pa Aroma 5:5, akunena kuti, "Ndipo chiyembekezo sichichititsa manyazi; chifukwa chikondi cha Mulungu chinatsanulidwam'mitima mwathu mwa Mzimu Woyera."Tere chikondi ichi, ndichimene Mulungu akuchilamulira kuti chiyenera kuonekera pakati pa akristu. Tamvani Paulo pa Aroma 5:8, akunenetsa kuti, "Koma Mulungu atsimikiza kwa ife chikondi chake cha mwini yekha m'menemo, kuti pokhala ife chikhalire ochimwa, Kristu adatifera ife."

Tsono nkhani ikuti, ndizoona kuti palibe m'modzi amene amafuna Mulungu, koma Mulungu mwini kudzera mwa Ambuye Yesu Kristu, anadza kudzafunafuna inu ndi ine.Ndiye tikunena kuti chomwe ine ndidziwa cha Mulungu ndicho chimene chionekera mwa Ambuye Yesu.Apa, ndikunena kuti ine sindidziwa chomwe Mulungu

amaganiza ndi chomwe Iye amamvapazinthu zina zikamachitika. Koma pamene tilondola moyo wa Ambuye Yesu Kristu, ndipo pamene tizindikira chomwe Mulungu amaganiza ndi kumvera pamene zinthu zina zichitika. Mwachitsazo ine ndimamva momwe Mulungu amamvera pamene ine, ndilira wokondedwa wanga. Pa Yohane 11:35, ndipamene tikumva kuti, “Yesu analira.” Komanso ndimadziwa momwe Mulungu amakondera ana, chifukwa Ambuye Yesu anawanyamula m’manja mwake ndi kunena kuti musatiletsetianatidzekwa Ine ndipo anatidalitsa. Tsono ndikudziwa zonsezi chifukwa Ambuye Yesu anadza m’dziko lino kudzaonetsa Mulungu.

Koma funso mkukhalapo kuti, kodi dziko loipalotere lomwe tikukhalamo, likhoza kudziwa Mulungu mwanjira yanji?Nkhani ikuti inu ndi ine, ngati anthu wokhulupirira, ndife amene tiri ndi udindo wouza dziko loipali za chikondi cha Mulungu.Mwachisoni kuti akristu ambiri lero lino, akuyesetsa kufuna kukondweretsa dziko loipali m’malo molalikira mau a Mulungu ku dzikoli. Tsono funso mkukhalapo kuti, kodi dzikoli limaganizanji za Ambuye Yesu Kristukomansolimaganiza chiyani za ife wokhulupirira, amene

timaimira Iye? Tikunena kuti palibe china chilichonse chomwe dziko limaganiziraife popeza tinamezedwa ndi dzikoli. Koma Uthenga ukuti inu ndi ine, tiyenera kupereka Uthenga wachipulumutso kudzikoli mwanjira yolalikira mau a Mulungu.Koma chinthu chofunika kwambiri chomwe dziko lisowa ndicho chikondi.Tikunena kuti dziko silidziwa chikondi, kotero kuti limangoganiza chikondi cha mkazi ndi mwamuna basi.Kutanthauza kuti dziko silidziwa chikondi cha Mulungu ayi. Kunena kuti anthu akunjawa samdziwa Mulungu, koma ayenera kumdziwa kudzera mwa ife. Ichi, ndichimene Yohane akutanthauza pamene akuti, “Mulungu akhala mwa ife ndi chikondi chake chikhala changwiro mwa ife.”

13. M’menemo tizindikira kuti tikhala mwa Iye, ndi Iye mwa ife, chifukwa anatipatsako Mzimu wake.

Ndime ino ndiyomwe ikutsimikiza kuti dziko silidziwa chikondi cha Mulungu, koma ife ndife tichidziwa, kupyolera mwa Mzimu Woyera amene akhala mwa ife. Kutanthauza kuti ichi, sichikondi cha Mulungu ayi ndipo kuti palibe munthu amene angakonze kuti akonde mnzake. Ndipo Paulo pa Agalatiya 5:22-23, adanena kuti,

“Koma chipatso cha Mzimu ndicho chikondi, chimwemwe, mtendere, kuleza mtima, chifundo, kukoma mtima, chikhulupiriro, chifatso, chiletso; pokana zimenezi palibe lamulo.” Tere pamndanda umenewu, inu mukhoza kuona kuti chikondi ndichimene chikutsogola, kotero kuti anthu akunja ambiri ayembekeza kuona chikondichi m’moyo wa akristu. Mwachisoni kuti akristu saonetsachikondichipopeza ichi,ndichiphunzitso china chomwe sichikuperekedwa pakati pa akristu.Kodi mumpingo mwanu, mwaphunzitsidwakangati phunziro la chikondi?

Wokondedwa anzanga apaulendo, tikunena kuti pamene chikondi chionekera m'nyumba, sipafunikansokuuzidwa kuti mkazi ayenera kuchita izi ndi izi. Komanso mwamuna sayenera kuuzidwa kuti akonde mkazi wake ayi. Zonsezi zimachitika monga momwe kuyenera chifukwa cha chikondi cha Mulungu.Kutsimikiza kuti chikondi cha Mulungu ndichodabwitsa kotero kuti chiyenera kuti chionekere mwa ana ake pamene akondana wina ndi mnzake.

Tsono pamene Yohane akunena kuti, “M’menemo tizindikira kuti tikhala mwa Iye, ndi Iye mwa ife, chifukwa anatipatsako Mzimu wake,” akutanthauza kuti inu ndi ine, sitingathe kupanga chikondi

chotere pa ife tokha ayi. Ichi, ndichimene chandikumbutsa verse 4, lomwe likuti, “Pakuti Iye wakukhala mwa inu aposa iye wakukhala m’dziko lapansi.”Mau awa, akunena kuti wokhulupirira ndiwo wodzazidwa ndi Mzimu Woyera ndipo Mzimu Woyera ndiye amalonga chikondi mumtima mwa mkristu.Kutsimikiza kuti ndizosatheka kuti ine pa ine ndekha ndipange chikondi.Ndikunena mau amenewa chifukwa moyo wamunthu aliyense unapotokerakuudani.Taonani munthu wina akamenya mnzake, nthawi yomweyo winayo amafuna kubwezera.Kodi inu mulibe mwa inu mtima wobwezera? Ndiye tikunenetsa kuti pamene Mzimu Woyera akhala mwa ife, chikondi cha Mulungu chidzaonetsedwa kudziko lonse popeza sipadzakhalakubwezeraudani.

14. Ndipo ifetapenyera, ndipo tichita umboni kuti Atate anatuma Mwana akhale Mpulumutsi wa dziko lapansi.

Uwu, ndiuthengawaumboni.Tikunena kuti inu ndi ine ngati anthu wokhulupirira, tiyenera kupereka Uthenga umenewu. Kunena kuti tiyenera kupereka Uthenga wachipulumutso kwa ena, ichi ndicho cholinga cha chikondi. Ndifuna kubwerezanso kuti, pamene tikamba nkhani yachikondi sitikunena chikondi chapakati pa

mwamuna ndi mkazi kapena chikondi chongoonetsakusangalala ndi munthu wina ayi.Ichi, ndichikondi chomwe chimaonekera chokha pamene titenga ndi kupereka Uthenga kudziko la anthu otaika.Ichi, ndichikondi chomwe ndichobvutakuchimvetsa. Tikaonetsetsa tipeza kuti atumiki a Mulungu amakumana ndi zobvuta zambiri pamene atengera Uthenga Wabwino kwa anthu amene ndiwobvutakuwakonda. Ndiye chimene chimakakamiza atumikiwa ndi chikondi chomwe alinacho panthawiyo.Kutanthauza kuti chikondi ichi, sichiona momwe munthu aonekera, akuchokera, komanso kuti mtundu wake ndani?Kodi inu mudayambamwakhala nacho chikondi choterechi?

15. Iye amene adzabvomereza kuti Yesu ali Mwana wa Mulungu, Mulungu adzakhala mwa iye ndi iye mwa Mulungu.

Pano ndifuna kubwerezanso kuti chiphunzitso choona ndichomwe chimaonetsa kuti Yesu Kristu ndi Mwana wa Mulungu. Kutsimikiza kuti kubadwa kwa Yesu mwa namwali, ndikofunika kwambiri. Tsono Paulo akunena za Uthenga Wabwino pa 1 Akorinto 15:3-4, pamene akuti, “Pakuti ndinaperekakwa inu poyamba, chimenensondinalandira, kuti Kristu anafera zoipa

zathu, monga mwa malembo; ndi kuti anaikidwa; ndi kuti anaukitsidwa tsiku lachitatu, monga mwa malembo." Ndiye funso likuti, kodi Uthenga wakuti Kristu anafa ndi kuukitsidwa, ukanakhalawomveka, ngati Kristuyo akadapanda kubadwa monga munthu?Tikunena kuti tiri ndi umboni wonse wakuti Yesu Kristu anabadwa mwa namwali. Kutsimikizadi kuti Yesu Kristu anali kunena zoona kuti ndiye Mwana wa Mulungu.

Tsono pamene Yesu akunenetsa kuti ndiye Mwana wa Mulungu, akutanthauza kuti Mzimu wa Mulungu akhala mwa Iye, kotero kuti ndiye Mulungu yemwe.Ichi, ndichifukwa chake Ambuye Yesu adanena kuti, "Chilichonse chimene Atate achita, Ine ndichita."Ndiye tamvani mau ya Ambuye Yesu yochititsa chidwi omwe adanena pa Yohane 5:24, pamene adati, "Indetu, indetu ndinena kwa inu, kuti iye wakumva mau anga ndi kukhulupirira Iye amene ananditumа Ine, ali nawo moyo wosatha, ndipo salowam'kuweruza, koma wachokerakuimfa."Tsono funso likuti, kodi ndizotheka bwanji zimenezi? Taonani Ambuye Yesu wangonenakumene pa Yohane 5:19, kuti, "Indetu, indetu ndinena kwa inu, sakhoza Mwana kuchita kanthu pa yekha, koma chimene

aona Atate achichita ndicho." Mwa mau amphamvu amenewa, tikunenetsa kuti Yesu Kristu adzaukitsa akufa onse ndipo adzawaweruza. Ichi, akunena kwa inu ndi ine chifukwa Iye ndiye anabadwa nafa komanso kuuka kwa akufa. Ndipo lero lino ngati mutamva mau ake, ndikumkhulupirira, inu mudzapulumuka ndithu.

16. Ndipo ifetazindikira, ndipo takhulupirirachikondicho Mulungu ali nacho pa ife. Mulungu ndiye chikondi, ndipo iye amene akhala m'chikondi akhala mwa Mulungu ndipo Mulungu akhala mwa iye.

Mau ali mundime iyi, akuonetsa kulukana kapena m'gwirizano wa zinthu ziwiri; zomwe ndi "chikondi" komanso "kukhala mwa Mulungu."Tikunena kuti zinthu ziwirizi zimayendera pamodzi, kotero kuti ndikobvuta kunena kuti inu mukonde Mulungu pamene simukonda m'bale.

Wokondedwa anzanga apaulendo, tikunena kuti pali chiyanjano chachikulu pakati pa Mulungu ndi munthu amene akonda cholengedwa cha Mulungu. Kutsimikiza kuti munthu amene akhala m'chikondi chopatulika, akhaladi m'chikondi cha Mulungu

chomwe chikhala pamtima pake. Mzimu wa Mulungu ndiwomweumamupatula ndi kusindikiza moyo wake kukhala wodalira pemphero kotero kuti amalira kukakhala ndi Ambuye nthawi zonse.Kodi inu mulinachochilakolako chimenechi?

17. M'menemo chikondi chathu chikhala changwiro kuti tikhale nako kulimbika mtima m'tsiku la mlandu; chifukwa monga Iyeyu ali momwemo tiri ife m'dziko lino lapansi.

Pano pali nkhani yochititsa chidwi chifukwa ikuti, chikondi cha Mulungu mwa ife chikhala changwiro ndi cholinga chakuti tikakhale nako kulimbika mtima patsiku la mlandu. Kunena kuti chikondi chimenechi chidzatikonzekeretsaife kukhala wolimbika mtima kukafikakumpando wakuweruza. Ndiye Yohane akunenetsa kuti izi, zidzachitika motere chifukwa moyo wathu m'dziko lino, ndiwo wofanana ndi wa Kristu. Kutsimikiza mau akuti munthu amene ali ndi chikondi choona chapa Mulungu, sadzaopa kanthu patsiku la chiweruzo, kotero adzafikakumpandowoopsa wakuweruza molimbika mtima kuti akalandirechomuyenera cha moyo wake wonse.

18. Mulibe mantha m’chikondi; koma chikondi changwirochitaya kunja mantha, popeza mantha ali nacho chilango, ndipo wamanthayo sakhala wangwiro mchikondi.
19. Tikondaife, chifukwa anayamba Iye kutikonda.

Ndime iyi, ikuti munthu mwachilengedwe chake ndi wamantha, koma mwana wa Mulungu sayenera kukhala ndi mantha ndi mlandu womwe ukudza chifukwa unaweruzidwa kale ndipo unatha pamene Kristu anafa m’malo mwanu ndi mwanga. Tere mkristu wamantha ndi chiweruzo chomwe chikudza m’tsogolo, ndiye amene alibe chimwemwe ndi chipulumutso chake.Pamau amenewa tikuti chimwemwe chimachokera kuchikondi, ndipo ngati inu muli ndi chikondi pa Ambuye Yesu Kristu, pa Mulungu ndi pa abale, ndizodziwikiratu kuti mantha achotsedwa. Koma tiyenera kudziwa kuti Mulungu ndiye anayamba kutikondaife. Tere tikunenetsa kuti Iye anakonda ife pamene tiri woipa wosakonzeka. Apa, ndipo pamene Mwana Wankhosa ayenera kulandira ulemu ndi matamando.

20. Munthu akati, kuti ndikonda Mulungu nadana naye m’bale wake, aliwabodza, pakuti iye wosakonda m'bale wake amene wamuona, sakhoza kukonda Mulungu amene sanamuona.
21. Ndipo lamulo ili tiri nalolocokera kwa Iye, kuti iye amene akonda Mulungu akondenso m’bale wake.

Mtumwi Yohane akunena kuti ngati inu munena kuti mumakonda Mulungu, mudana ndi m’bale wanu, ndiye kuti ndinu wabodza.Apa, ndipo pamene pakumdza funso lakuti, kodi ndizotheka bwanji kudana ndi m’bale wako amene umuona, ndi kukonda Mulungu wosaonekayo? Izi, ndizosatheka, kotero kuti ndichifukwa chake lero lino anthu amadzionetsa kukhala wolungama ndi woyera mtima.Tikunena kuti m’mipingo yathu yambiri, muli Mzimu umenewu wachinyengo.Ndiye tikunena molimba mtima kuti ngati inu simukonda m’bale wanu amene mumpenya, ndiye zikutsimikiza kuti inu simukondanso Mulungu.

Wokondedwa anzanga apaulendo, tiyeni titsirize ndi mau akuti Mulungu akulamula kuti wokhulupirira aliyense, akondane ndi m’bale wake.Nkhani iyi, ikutanthauza kuti inu simukupatsidwa mwayi wakuti mukhoza kukonda ngati mungafune ayi, koma

mukulamulidwa kukonda m'bale wanuyo. Taonani Mulungu akupereka ulamuliro umenewu kuti popeza Iye atikondaife, ifenso tiyenera kukonda abale athu. Kodi inu mulinacho chikondi chotere pa abale anu?Kapena tifunse kuti, kodi inu mumachita monga Mulungu alamula inu kuchita?

Kwalerotilekeza pano. Koma tinali kukambairana kuchokera pa 1 Yohane 4:12-21, pomwe timapitiliza mutu wakuti wokhulupirira ayenera kukondana wina ndi mnzake.

Ambuye akudalitseni inu lero. Amen!